Examination No: ____________________

# NORTHERN EDUCATION DIVISION

## 2026 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMINATION

## CHICHEWA

(Malikisi 100)

**Tuesday, 24 March** **Subject number: P032**

**Time Allowed: 2h 15 mns**

**1:00 – 3:15 pm**

**Dzina lanu:** ____________________

**Dzina la sukulu yanu:** ______________ Zone yanu: ____________ Boma lanu:____________

**Malangizo**

1. **Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa asanu ndi atatu.**
2. Pepala ili lili ndi magawo anayi: Gawo **A, B, C** ndi **D.**
3. Lembani **dzina** lanu ndi **dzina la sukulu** yanu pamwamba patsamba lino.
4. Lembani nambala ya mayeso pa mwamba pa tsamba lililonse.
5. Lembani chimangirizo kapena kalata mu **Gawo A** ndipo muyankha mafunso onse mu **Gawo B, C** ndi **D**.
6. Muchitebulo chili pambalichi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lilikutsogolo kwake
7. Perekani kwa okuyang'anirani kulemba mayeso (**Imvijireta**) pepala lonseli nthawi ikakwana.

| Funso | Chongani zomwe mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6-10 | | | |
| 11-15 | | | |
| 16-17 | | | |
| 18-20 | | | |
| 21-25 | | | |
| 26-28 | | | |
| 29-33 | | | |
| 34-38 | | | |
| 39-42 | | | |
| 43-45 | | | |

© 2026 NED PSLCE MOCK

Turn over

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

## GAWO LOYAMBA (30 MALIKISI)

**Langizo**:Yankhani funso **limodzi** lokha mwa mafunso ali m'munsimu. Sankhani mutu wa chimangirizo **kapena** wa kalata. Mawu a **chimangirizo** chanu kapena **kalata** yanu asachepere **100** koma asabzole **150**.

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu:

   **ZOKHUMBA ZANGA**

   Mwa zina za mfundo zanu tsatirani izi polemba:

   **Ndime yoyamba**
   - Zomwe mukufuna kudzakhala.
   - Chifukwa chomwe mukufunira kudzakhalacho.

   **Ndime yachiwiri**
   - Zomwe mukuchita kuti mukwaniritse zokhumba zanu.
   - Amene akuthandizani kuti mukwaniritse zokhumba zanu.

   **Ndime yachitatu**
   - Zomwe mudzachite mukadzakwaniritsa zokhumba zanu.

**KAPENA**

2. Lembani kalata kwa atsibweni anu yowadziwitsa kuti mwasankhidwa kupita ku sekondale yogonera konko.

   Mwa zina tsatani izi polemba:

   **Ndime yoyamba**
   - Kusukulu komwe mwasankhidwira.
   - Zomwe munachita kuti musankhidwe.

   **Ndime yachiwiri**
   - Masomphenya amene muli nawo pa nkhani ya sukulu.
   - Yemwe adatengapo gawo lakuthandizani kuti musankhidwe.

   **Ndime yachitatu**
   - Chisangalalo chomwe mudzakhale nacho mukakwaniritsa masomphenya anu.

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

## GAWO B: KUMVETSA NKHANI (MALIKISI 20)

**Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawo.**

Kalekale chakum'mawa kwa mtsinje wa Kalolo kudali mudzi wina wotchedwa Mala M'mudzimo mudali banja lina lomwe lidali ndi ana atatu; Zwane, Gwane ndi Zwita yemwe ad chitsekamawere.

Anawa adali omva mwambo, ngakhale Zwita adali wovutirapo yemwe adali mwana wamka yekhayo popeza adali okonda anyamata. Tsiku lina m'mudzimo mudali mchezo wa khirisimas Zwita ndi abale ake sadabwerere m'mbuyo. Kumalo otere samafuna kuti ziwadutse. Adanyamuk nthawi ya usiku kuti nawonso akadziwonere wokha. Paja zakumva ziphweteketsa mutu, Zwit adapezana ndi anzake nawo a kamwendo mnjira, machezo awo adayenda bwino.

Zwane ndi Gwane adaganiza zobwerera kunyumba nthawi ya usiku koma Zwita adatemets nkhwangwa pa mwala kuti sangabwerere nthawi imeneyo. Zwita adakhaladi ndipo adapitiliz macheza ake.

Kuli mbuu kunja Zwita adaganiza zobwerera kunyumba. Ali mnjira yekhayekha adadabwa atakumana ndi chinthu chozizilitsa nkhongono. Adachita mantha nayamba kuthawa uku akulira mokweza. Adayetsetsa kuliyatsa la mtondo wadooka mpaka adafika kunyumba kwa makolo ake. Makolo ake adamuona adamulandira ndipo adamukumbutsa kuti sibwino kukhala mwana wosamvera ndipo sakuyenera kumayenda usiku ngati mwana wamkazi iyeyo.

Zwita adamvera makolo ake kuchokera pomwepo adasintha khalidwe lake nakhala mwana wabwino zimenezi zidamuthandizira kulimbikira maphunziro ake ndipo adaphunziradi mpaka ku sukulu ya ukachenjede. Adaphera mphongo kuti phukusi la moyodi umasunga wekha.

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizele ili pansi pa funso lililonse.**

3. (a) Kodi banja lomwe linali ndi ana atatu limachokera m'mudzi wanji?

______________________________ (Malikisi 1)

(b) Tchulani dzina la mwana wa mkazi yomwe adali ovuta.

______________________________ (Malikisi 1)

(c) Fotokozani khalidwe la Zwita

______________________________ (Malikisi 2)

______________________________

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

(d) Pezani mawu ofanana ndi 'mzime' kuchokera mu nkhaniyi.

______________________________ (Malikisi 1)

(e) N'chifukwa chiyani anawa adachoka pakhomo pa makolo awo nthawi ya usiku?

______________________________

______________________________ (Malikisi 2)

(f) Mawu oti 'kamwendo mnjira' amatanthauza chani?

______________________________

______________________________ (Malikisi 1)

(g) Pezani mawu mnkhaniyi omwe akutanthauza 'kukanitsitsa'

______________________________

______________________________ (Malikisi 2)

(h) Nchifukwa chiyani Zwita analira?

______________________________

______________________________ (Malikisi 2)

(i) Perekani langizo lomwe makolo a Zwita adamupatsa

______________________________

______________________________ (Malikisi 2)

(j) Lembani m'kuluwiko iwiri yomwe yagwiritsidwa ntchito mnkhaniyi.

i. ______________________________

______________________________ (Malikisi 1)

ii. ______________________________

______________________________ (Malikisi 1)

(k) Kodi malangizo omwe adamupatsa makolo ake adamuthandiza bwanji Zwita.

______________________________

______________________________ (Malikisi 2)

(j) Pezani mutu wa nkhaniyi

______________________________ (Malikisi 2)

## GAWO C :(MALIKISI 10)

**Yankhani mafunso awiri m'gawoli**

4. Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.
"Popeza mwayamba kale kulongosola, koma zoona zake ndi zoti mnyamatayu ndi wazala zazitali. Mosataya nthawi igwa apa ndi mbuzi ziwiri."

**Mafunso:**

(a) Ndi malonje anji amenewa?

______________________________ (Malikisi 1)

(b) Ndani akuyankhula m'malonjewa?

______________________________ (Malikisi 1)

(c) Perekani tanthauzo la mawu awa "zala zazitali."

______________________________ (Malikisi 1)

(d) Lembani njira ziwiri zotumizira uthenga wamaliro

______________________________

______________________________ (Malikisi 2)

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

5. Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:
(a) Hehede! ______ (Malikisi 1)
(b) denga ______ (Malikisi 1)
(c) pita ______ (Malikisi 1)
(d) wamtali ______ (Malikisi 1)
(e) lero ______ (Malikisi 1)

## GAWO D: (MALIKISI 40)

Zungulizani lembo lokhoza **(A, B, C kapena D)** m'mafunso otsatirawa:

**Mafunso 6 mpaka 10:** Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi:

6. Mnyumba muno aliyense ndi mnzanga.
   A. mfotokozi C. muonjezi
   B. mlowammalo D. mperekezi

7. Lero tidyera nsomba zaziwisi.
   A. dzina C. mfotokozi
   B. muonjezi D. mneni

8. Kwa eni kulibe mkuwe.
   A. mneni C.mfotokozi
   B. muonjezi D. mperekezi

9. Dalitso wakumba nkhuti.
   A. mneni C. mfotokozi
   B. mperekezi D. mounjezi

10. Kulima ndi kwabwino.
   A. mneni C. dzina
   B. mfotokozi D. muonjezi

**Mafunso 11 mpaka 15:** Sankhani matanthauzo a zining'a zomwe zatsekedwa mzere:

11. Akazi awo ali ndi kaduka ka chinangwa.
   A. kachiduka
   B. munda wa chinangwa
   C. nsanje yayikulu
   D. mantha aakulu

12. Bambo Phiri adagwerula nkhwangwa ndi cham'mbuyo.
   A. wobereka C. wolemera
   B. wosabereka D. wosauka

13. Chimwemwe ndi waziwala mmaso.
   A. wachikondi C. wopenyapenya
   B. wachimasomaso D. wamisala

14. Iye anadya matako a galu.
   A. Okonda kuweta galu
   B. woyendayenda
   C. woyelekedwa
   D. wodzikonda

15. A Nambewe adataya udzu omwetamweta chifukwa cha nsanje.
   A. kuchita mwayi C. kumwalira
   B. kuchita tsoka D. kutaya mwayi

**Mafunso 16 mpaka 20:** Sankhani mitundu ya wa msintho wa aneni omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatira:

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

16. Nyumbayi yamangika bwino.
A. wapoyera
B. wamchibisira
C. wonyazitsa
D. womchitira

17. Amayi alumwa ndi njoka.
A. Wochitidwa poyera
B. womchitira
C. wochitirana
D. wonyazitsa

18. Asing'anga atsirikula munda.
A. womchitira
B. wochitirana
C. wotsutsa
D. wamchibisira

19. Iwo apatsana moni dzulo.
A. wochitirana
B. womchitira
C. wochititsa
D. wamchibisira

20. Mateyu wathawitsa ng'ombe.
A. wochitititsa
B. wobwerezabwereza
C. wochititsa
D. womchitira

**Mafunso 21 mpaka 25:** Sankhani chachikazi chamayina awa:

21. Mphulu.
A. nkhuku
B. nkhosa
C. nkhosa
D. mbuzi

22. Nthondo.
A. ntchowa
B. mdzakazi
C. mfumukazi
D. mumphwa

23. Mphwako
A. mfumakazi
B. mkamwini
C. mtengwa
D. mtsibweni

24. Tambala.
A. chipsolopsolo
B. msoti
C. nkhuku
D. thadzi

25. Mkamwini
A. wakunjira
B. mtengwa
C. phungu
D. mlendo

**Mafunso 26 mpaka 30:** Sankhani ntchito za 'ndi' yemwe watsekedwa nzere kunsi.

26. Mudzi wa Kanyenda ndi wa mtendere.
A. kukhala mperekezi
B. kukhala mneni
C. kukhala mvekero
D. kukhala mlumikizi

27. Amayi akugulitsa nsawawa ndi mtedza.
A. kukhala mlumikizi
B. kukhala mneni
C. kukhala mlowam'malo
D. kukhala mperekezi

28. Ine ndifuna mwana waulemu.
A. kukhala mneni
B. kukhala mperekezi
C. kukhala mlowammalo
D. kukhala mlumukizi

29. Amayi ali ndi ana awo.
A. kukhala mperekezi
B. kukhala mneni
C. kukhala mlowammalo
D. kukhala mlumikizi

30. Nsimayo yalimba kuti ndi.
A. kukhala mperekezi
B. kukhala mvekero
C. kukhala mneni
D. kukhala mlumikizi

**Mafunso 31 mpaka 35:** Sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro za mkalembedwe zoyenera:

31.

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

2026

A. Ha! Mwanawe, andithangate ndani?
B. Ha! Mwanawe andithangate ndani.
C. Ha! Mwanawe andithangate ndani?
D. Ha! Mwanawe? andithangate ndani?

32.
A. Tadala amayenda, monyada.
B. Tadala amayenda monyada.
C. Tadala, amayenda monyada
D. Tadala, amayenda monyada.

33.
A. Undipatse mtedza adatero atate.
B. "Undipatse mtedza", adatero atate.
C. Undipatse mtedza "adatero atate".
D. Undipatse mtedza, adatero atate.

34.
A. Wagula Nyemba ndi Mtedza.
B. Wagula nyemba ndi mtedza.
C. Wagula nyemba ndi Mtedza
D. wagula nyemba ndi mtedza.

35.
A. Mwanawe, uzilimbikira sukulu.
B. Mwanawe! uzilimbikira sukulu.
C. Mwanawe uzilimbikira sukulu.
D. Mwanawe, uzilimbikira Sukulu.

**Mafunso 36 mpaka 40:** Sankhani mawu ofanana m'matanthauzo ndi omwe mwapatsidwa munsiwa.

36. Adatenga chikwerete kwa bambo Bengo.
A. msonkho C. ngolo
B. ng'ombe D. ngongole

37. Wagwira kapeta.
A. kakowa C. pusi
B. kabwanda D. mbalame

38. Nyantha bango ili.
A. meza C. yamwa
B. seteka D. luma

39. Amakonda kudya chimungulu.
A. mbatata C. mtedza
B. chinangwa D. bowa

40. Lero ndaona chidude.
A. wakuba C. woledzera
B. wamisala D.mzukwa

**Mafunso 41 mpaka 45:** Sankhani mtundu wa nthambi yomwe yatsekedwa mzere kunsi kwawo:

41. Umuuze kuti abwere mawa.
A. ya muonjezi C. yamfotokozi
B. ya dzina D. yoyima payekha

42. Sindidzabweranso pokhapokha mudzanditenge.
A. ya muonjezi C. yadzina
B. ya mfotokozi D. yoyima payokha

43. Walipeza khasu limene linasowa dzulo.
A. yoyima payokha
B. ya muonjezi
C. ya dzina
D. ya mfoktokozi

44. Zomwe mukuchita ndazidziwa.
A. ya dzina C. yamuonjezi
B. yoyima payokha D. ya mfotokozi

45. Zoti ndiwabodza ndikudziwa.
A. ya dzina C. ya mfotokozi
B. yoyima payokha D. ya muonjezi

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com